Kodi chinthu choyamba chimene Yesu anatumira ophunzira kunja kukachita chinali chiyani?

(1) ______________________________

(2) Kukachiza anthu.

==================================================================

15. Iye anaŵatuma kuti akalalikire Ufumu wa Mulungu. Iye anaŵapatsa mphamvu kuti apose ziwanda ndi kuchiza matenda. Iye anaŵauza kuti zosoŵa zidzasamalidwa. Akuphunzira anachita zimene Yesu ananena. Ngakhale mfumu inamva zomwe iwo anali kuchita. Zinthu zimene anali kuchita zinapanga kuti Herode afune kuona Yesu. Zinthu zimene amachita ziyenera kukopa anthu kuti afune kudziŵa zina zambiri za Yesu.

Luka 9:7,9:

> Ndipo Herode chiŵangacho anamva mbiri yake ya zonse zinachitika; ...Ndipo anafunafuna kumuona Iye.

Pa Luka 9:2, kodi Yesu anatumiza ophunzira khumi ndi aŵiri kunja kuti akachite chiyani?

(1) Kukalalikira Ufumu wa Mulungu.

(2) ______________________________

==================================================================

16. Iye anaŵatuma kuti akalalikire ndi kukachiritsa anthu. Ophunzira anachita monga momwe Yesu anaŵauzira kuti achite. Ifenso lero tiyenera kumachita zinthu zomwezi.

Luka 9:6:

> Ndipo iwo anatuluka, napita m'midzi m'midzi ndi kukalalikira Uthenga Wabwino, ndi kuchiritsa ponse.

Kodi mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani sitimaona anthu ambiri ali kuchiritsidwa masiku ano?

______________________________

==================================================================

17. Tidzakambirana za izi tonse pamodzi.

Luka 9:2: Kodi Yesu anatumiza ophunzira khumi ndi aŵiri kunja kuti akachite chiyani?

(1) ______________________________

(2) ______________________________

==========================================================================

SABATA LA KHUMI: KHRISTU, MKATE WA MOYO
TSIKU LOYAMBA: IYE ANADYETSA ANTHU ZIKWI ZISANU

1. Sabata lapita tinaona mmene Yesu anaphunzitsira anthu ambiri. Iye mwini anaŵaphunzitsa. Iye anatumiza khumi ndi aŵiri kunja. Sabata ino tiona mmene amaperekera moyo kwa anthu tsiku lililonse.

Pa Luka 9:2, kodi Yesu anatumiza ophunzira khumi ndi aŵiri kuti akachite chiyani?

(1) ____________________

(2) ____________________

==========================================================================

2. Iye anatumiza ophunzira kuti atuluke kunja kukalalikira Ufumu wa Mulungu, ndi kukachiritsa anthu. Lero tiphunzira za chozizwitsa chachikulu cha Yesu. Iye anadyetsa anthu zikwi zisanu!

Yesu ndi ophunzira ake anapita kumalo apadera kukapumula. Koma anthu ambiri anaŵatsata kumalo amenewo. Yesu analankhula kwa iwo kwa nthaŵi yaitali. Nthaŵi nkuti itatha ndipo anthu anali kufuna chakudya. Tsiku limenelo Yesu anachita zozizwitsa. Iye anadyetsa anthu zikwi zisanu. Chozizwitsa chimenechi chimatiphunzitsa zinthu ziŵiri za Yesu.

(1) Yesu anakonda anthu
(2) Yesu ali ndi mphamvu yaikulu.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Marko 6:34-44. Kodi inu munayamba mwamva gulu la anthu lokwana zikwi zisanu litasonkhana pamalo amodzi?

____________________

Kodi anthu zikwi zisanu ndi ambiri kapena ochepa? ____________

==========================================================================

3. Mwina inu munaona anthu zikwi zisanu akuonera mpira mumzinda waukulu Anthu okwana zikwi zisanu ndi anthu ambiri. Buku Lopatulika limanena kuti anthu ambiri otere anadza kwa Yesu.

Marko 6:34:

Ndipo anatuluka Iye, naona khamu lalikulu la anthu, nagwidwa chifundo ndi iwo.

Yesu anadziŵa kuti ambiri mwa anthu ameneŵa sanali kutsatira Mulungu. Iye anafuna kuwaphunzitsa zinthu zambiri za Mulungu.

Kodi ndani amene anali ndi chikondi cha pa gulu lalikulu la anthu?

__________________________________________

===============================================================

4. Ndi Yesu amene anachita zimenezi. Ife timaphunzira zinthu zambiri kuchokera ku chozizwitsa chimene Yesu anachitira anthu zikwi zisanu. Chinthu choyamba chimene timaphunzira ndi chakuti Iye amakonda anthu. Taonaninso ndimeyi.

Marko 6:34:

Ndipo anatuluka Iye naona khamu lalikulu la anthu nagwidwa chifundo ndi iwo.

Yesu anadziŵa kuti ambiri mwa anthu ameneŵa sanali kutsatira Mulungu. Iye anafuna kuŵaphunzitsa zinthu zambiri za Mulungu.

Kodi Yesu anagwidwa ndi chiyani mmene anaona anthu ambiri tsiku limenelo?

__________________________________________

__________________________________________

===============================================================

5. Iye anali ndi chikondi ndi anthu zikwi zisanu. Iye anasamalira zosoŵa zawo za uzimu. Ichi ndicho chifukwa chake chimene Iye anayamba kuŵaphunzitsa iwo zinthu zambiri za Mulungu. Koma Yesu anasamaliranso za zosoŵa za thupi. Iye ndi akuphunzira anabwera kumalo ameneŵa kudzapumula. Akuphunzira nkuti atangobwera kumalo ameneŵa kuchokera kokalalikira ndi kuchiritsa anthu. Iwo anali otopa. Yesu anafuna kuti iwo apumule.

Marko 6:31:

Ndipo Iye ananena nawo, "Idzani inu nokha padera ku malo achipululu, mupumule kamphindi."

Kuchokera m'ndime imeneyi, kodi timadziŵa bwanji kuti Yesu amasamalira zosoŵa za matupi athu?

______________________________

______________________________

==========================================================================

6. Yesu anafuna ophunzira kuti apumule. Koma anthu anadziŵa komwe Yesu anali kupita. Iwo anathamanga patsogolo pa Yesu ndi akuphunzira. Iwo ndiwo anayamba kukafika. Ndili kuganiza kuti akuphunzira anali okwiya pamene iwo anaona unyinji wa anthu onsewo. Akuphunzira anali kupita kuchipululuko kuti akapumule nthaŵi pang'ono. Koma pamene anaona anthu, Iwo anadziŵa kuti Yesu sakadakhoza kuŵapitikitsa.

Kodi Yesu akadaonetsa chikondi akanaŵathamangitsa? ______________

==========================================================================

7. Iye sakadaonetsa chikondi. Koma ophunzira anasoŵa kupumula. Kapena inu nthaŵi zina mumakhala ndi vuto limeneli. Mumafunika kupumula, kapena muli kufuna kukonzekera ulaliki. Pa nthaŵi yomweyo mlendo afika kunyumba kwanu. Kodi nthaŵi zina mumakhala wosakondwa? Ine nthaŵi zina ndimakhala wosakondwa ndi mlendo wofika nthaŵi imeneyi. Anthu amene amagwira ntchito ya Mulungu ayenera kupumula nthaŵi zina. Chimenechi chimatipatsa ife kukhala ndi mphamvu kuti tichite ntchito yambiri. Koma mwina mlendoyo ndi mbali imodzi ya ntchito yomwe Mulungu afuna kuti ife tichite. Kapena kuti ali ndi mavuto. Iye ali kufuna ife kuti tilankhule mawu a chikondi ndi mphamvu ya Mulungu kwa Iye.

Monga Yesu anaonetsa chikondi kwa anthu, kodi ife tiyenera kuonetsa chiyani kwa mlendo?

______________________________

==========================================================================

8. Ndili ndi chitsimikizo kuti inu mwavomera kuti Mulungu amafuna kuti ife tionetse chikondi. Pali nthaŵi zina zimene timakhala otanganidwa. Koma zimenezi ndi zovuta. Yesu anayesedwa pa nthaŵi imeneyi. Koma pamene Iye anaona anthu, anaiŵala zosoŵa zake. Iye mwansanga anaonetsa chikondi kwa iwo. Iye anayamba kulalikira kwa iwo.

Lembani chinthu choyamba chimene kudyetsa anthu zikwi zisanu chimatiphunzitsa ife za Yesu. Ndipo werengani chachiŵiricho.

(1) ________________________________________

(2) Yesu anali ndi mphamvu yaikulu.

==================================================================

9. Chinthu choyamba ndi chakuti chozizwitsa ichi chimatiphunzitsa kuti Yesu amakonda anthu. Koma sichinthu chokhacho chimene chikutiphunzitsa. Kudyetsa anthu zikwi zisanu kutiphunzitsa kuti Yesu ali ndi mphamvu yaikulu. Iye ali ndi mphamvu yosandutsa chakudya chochepa ndi kuchichulukitsa. Akuphunzira sanaganizire kuti Yesu angachite zimenezi.

Marko 6:35-36:

Ndipo pamene dzuŵa lidapendeka ndithu, anadza kwa Iye ophunzira ake, nanena, "Malo ano nga chipululu, ndi dzuŵa lapendeka ndithu; muwauze kuti amuke, aloŵe m'milaga akadzigulire okha kanthu kakudya."

Kodi Yesu ali ndi chiyani chomwe chingathandize anthu? ____________

==================================================================

10. Yesu ali ndi mphamvu. Koma Iye sanagwiritse ntchito mphamvu yake nthaŵi yomweyo. Taonani zomwe Yesu anauza akuphunzira.

Marko 6:37:

Koma Iye anayankha nati kwa iwo, "Apatseni kudya ndinu." Ndipo iwo ananena naye, kodi tikapita ife ndi kugula mikate ya pa marupiya atheka mazana aŵiri, ndi kuwapatsa kudya?"

Kodi akuphunzirawo anali ndi chakudya chopatsa anthu? ____________

Kodi iwo anayenera kuchita chiyani kuti apeze chakudya?

________________________________________

________________________________________

==================================================================

11. Akuphunzira analibe chakudya chopatsa anthu. Iwo anayenera kukagula chakudya. Iwo anauza Yesu kuti chikadawatengera ndalama zokwanira mazana aŵiri kuti adyetse unyinji wa anthu otere. K1.00 unali mtengo wa ntchito imene munthu wagwira pa tsiku limodzi m'nthaŵi ya Yesu. Akuphunzira anati chikadaŵatengera masiku mazana aŵiri kuti agwire ntchito pofuna kupeza ndalama zodyetsera unyinjiwo.

Kodi akuphunzira anali ndi mphamvu yothandiza anthu? ________________

Kodi ndani anali ndi mphamvu yoŵathandiza iwo? ________________________

==========================================================================

12. Akuphunzira analibe mphamvu yothandiza anthu. Iwo analibe chakudya. Analibe ndalama zogulira chakudya. Yesu yekha ndiye anali ndi mphamvu yoŵathandizira. Yesu anauza ophunzira kuti afunse anthu ngati wina ali ndi chakudya. Ophunzira anapeza mnyamata wamng'ono yemwe anali ndi mikate isanu ndi tisomba tiŵiri. Nsombazo zinali zochepa kwambiri. Mikate inali monga timandasi timene anthu amadya m'maŵa.

Kodi mikate isanuyo ndi nsomba ziŵiri zinali chakudya chambiri kapena chochepa?

________________________________________________

==========================================================================

13. Mikate isanu ndi nsomba ziŵirizo chinali chakudya chosakwanira unyinji wa anthu onsewo. Taganizirani mmene akuphunzira anadabwira. Yesu anauza anthu kuti akhale pansi ndipo tiona zimene Yesu anachita.

Marko 6:41:

> Ndipo Iye anatenga mikate isanuyo ndi nsomba ziŵirizo, nayang'ana kumwamba, nadalitsa, nagaŵa mikate; napatsa kwa ophunzira kuti apereke kwa iwo; ndi nsomba ziŵiri anagaŵira onsewo.

Kodi inu mukuganiza kuti Yesu akadapeza bwanji chakudya chodyetsa unyinji wa anthu zikwi zisanu?

____________________________________

==========================================================================

14. Tidzakambirana za yankho lanu m'kalasi. Koma kumbukirani kuti Yesu ndi Mulungu weniweni amene anadza ku dziko lino lapansi. Iye analenga dziko lonseli ndi mawu osagwiritsa ntchito kanthu kena polenga. Iye akhoza kusandutsa miyala kukhala mikate ngati atafuna. Iye akhoza kusandutsa mitengo kuti ikhale nsomba ngati atafuna. Kwa ine sichinthu chovuta kumvetsetsa kuti Yesu angachulukitse chakudya chochepa kukhala chambiri.

Pamene Yesu anachulukitsa chakudya chochepa kukhala chambiri, kodi Iye anaonetsa mphamvu yaikulu kapena yochepa? ______________

===========================================================================

15. Iye anaonetsa mphamvu yaikulu. Chakudyacho chinali chambiri kwa aliyense. Ndiponso chakudya china chambiri chinatsala onse atatha kudya.

Marko 6:42-43:

> Ndipo anadya iwo onse, nakhuta. Ndipo anatola makombo, mitanga khumi ndi iŵiri, ndiponso za nsomba.

Chozizwitsa cha kudyetsa anthu zikwi zisanu chimatiphunzitsa zinthu ziŵiri za Yesu. Kodi chachiŵiri ndi chotani?

(1) Yesu akonda anthu

(2) ______________

===========================================================================

16. Chinthu chachiŵiri chomwe limatiphunzitsa ndi chakuti Yesu ali ndi mphamvu yaikulu. Anthu ena ali ndi mphamvu koma iwo sasamala za anthu ena. Iwo sagwiritsa ntchito mphamvu yawo kuti athandize.

Kodi ndi chinthu choyamba chotani chomwe kudyetsa anthu zikwi zisanu chimatiphunzitsa za Yesu?

(1) ______________

(2) Yesu ali ndi mphamvu yaikulu.

===========================================================================

17. Yesu amakonda anthu. Iye ali ndi mphamvu yaikulu. Ife timaona mphamvu zimenezi kupyolera ndi mmene anadyetsera anthu zikwi zisanu. Pamene ife tikuwerenga chimenechi m'Buku Lopatulika timakumbukira mmene Yesu anakhalira pa dziko lapansi. Nthaŵi zina ife timaiwala kuti Yesu ali ndi zinthu ziŵirizi. Iye adzatithandiza ife ngati timukumbukira.

Tsopano ganizirani za vuto lalikulu m'moyo wanu. Ngati mulibe mavuto olimba, ganizirani za limene munali nalo kale. Lembani za vuto limenelo pano.

______________________________________________

______________________________________________

Tsopano ganizirani za Yesu. Kodi muli kuganiza kuti Yesu akhoza kukuthandizani motani ndi vuto limenelo?

______________________________________________

______________________________________________

==================================================

18. Tidzakambirana za izi tonse pamodzi. Ngati inu simufuna kukamba za mavuto anu m'kalasi, mukhoza kulankhula ndi mtsogoleri wanu pakutha pa kalasi.

Kodi ndi zinthu ziŵiri zotani zimene chozizwitsa cha kudyetsa anthu zikwi zisanu chimatiphunzitsa ife za Yesu?

(1) ______________________________________________

(2) ______________________________________________

==================================================

SABATA LA KHUMI: KHRISTU, MKATE WA MOYO
TSIKU LACHIŴIRI: IYE ANAYENDA PA NYANJA NDI KUTONTHOLETSA NAMONDWE

1. Dzulo tinaphunzira zinthu ziŵiri kuchokera pa chozizwa chodyetsa anthu zikwi zisanu. Kodi ndi zotani?

(1) ______________________________

(2) ______________________________

==========================================================================

2. Kuchokera mu chozizwitsa chimenechi tinaphunzira kuti Yesu amakonda anthu. Tinaphunziranso kuti Iye ali ndi mphamvu yaikulu. Lero tiphunzira zozizwitsa zina ziŵiri. Taona kale kuti Yesu anali ndi mphamvu pa chilengedwe. Pa nthaŵi ina mphepo inavutitsa ophunzira. Yesu anali kubwera ali kuyenda pamadzi. Ndipo Iye analetsa mphepoyo. Yesu anali kulola kuti ophunzira akhale ndi mavuto kuti akhoza kuwaphunzitsa bwino. Iye masiku ano afuna kutiphunzitsanso chinthu chomwecho. Pamene tili m'mavuto a akulu:

(1) Yesu adzakhala nafe
(2) Sitiyenera kuchita mantha

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndipo werengani Marko 6:45-52. Kodi ndi vuto lotani linalepheretsa ophunzira kuti asaoloke nyanja?

______________________________

==========================================================================

3. Mphepo yaikulu inalepheretsa ophunzira. Inaŵapatsa vuto lambiri. Iwo sanathe kufika tsidya lina la nyanja. Dzulo tinaona kuti Yesu anafuna ophunzira ake kuti apumule. Phunziro la lero likudza pamene Yesu atangodyetsa anthu zikwi zisanu. Apanso Yesu anafuna kuti ophunzira apumule. Iye anaŵauza kuti atsogole. Iwo anamvera. Iwo anapita mngalawa. Yesu anatsala kuti atumize anthu kwawo ndi kulaŵirana nawo.

Marko 6:45:
Ndipo pomwepo Iye anakangamiza ophunzira ake alowe mngalaŵa, ndi kumtsogolera kutsidya lija ku Betsaida, mmene Iye yekha ali mkuuza khamulo kuti amuke.

Kodi ndi ndani anatumiza ophunzira tsidya lina la nyanja pa ngalawa?

______________________________________________

==================================================================

4. Yesu ndiye anachita zimenezi. Ndipo Iye anadyetsa anthu zikwi zisanu. Ndipo potsiriza anapita kuphiri kukapemphera payekha. Pamene Iye anapemphera, anaona ophunzira.

Marko 6:47-48:

> Ndipo pofika madzulo ngalawa inali pakati pa nyanja ndi Iye yekha pamtunda. Ndipo pakuŵaona ali kuvutika ndi kupalasa, pakuti mphepo inadza nikomana nawo, paulonda wachinayi wa usiku, Iye anadza kwa iwo, ali kuyenda pamwamba pa nyanja.

Pamene Yesu anaona kuti ophunzira ali m'mavuto, kodi Iye anachita chiyani?

______________________________________________

==================================================================

5. Yesu anapita kwa ophunzirawo. Iye anali kubwera ali kuyenda pamadzi Chimenechi ndi chozizwitsa choyamba chomwe Iye anathandiza iwo pa nthaŵi imeneyi. Yesu anafuna kudza kwa iwo. Iye anafuna kuthandiza mavuto awo. Kuchokera mu chozizwitsa ichi timaphunzira kuti Yesu amafuna kudza pafupi nafe. Iye adzakhala pafupi nafe pamene tili ndi mavuto a akulu.

Kodi ndi vuto lotani limene linaoneka kwa ophunzira pamene Yesu anadza kwa iwo pamadzi?

______________________________________________

______________________________________________

==================================================================

6. Iwo anali mu mphepo yaikulu. Iwo sakadakhoza kupitirira ndi ngalawa Yesu anaona vuto ndipo Iye anadza kwa iwo. Poyamba ophunzirawo anali kuchita mantha. Koma pamene Iye anadza pafupi ndi iwo anakhoza kuona kuti ndani. Iwo anaona kuti Iye anafuna kuŵathandiza. Ndipo Yesu anachita chozizwitsa chachiŵiri. Yesu anatontholetsa mphepo yaikuluyo. Ophunzira analeka kuchita mantha. Kuchokera mu zimenezi tikuphunzira

kuti ife sitiyenera kukhala amantha pamene mavuto adza kwa ife.

Kodi Yesu amakhala kuti pamene ife tiri m'mavuto? ____________

____________

========================================================================

7. Yesu ali ndi ife. Nthaŵi zina timakhala ndi mavuto ngakhale tiri omvera. Yesu anauza ophunzira kuti apite tsidya lina la nyanja pa ngalawa. Iwo anachita zimene Yesu anaŵauza kuti achite. Koma pasanapite nthaŵi mavuto anadza kwa iwo.

Marko 6:48:
Ndipo pakuŵaona ali kuvutika ndi kupalasa,
pakuti mphepo inadza nikomana nawo.

Kuchokera pa nthaŵi imene Yesu anayenda pamadzi, kodi chinthu choyamba ndi chotani chimene timaphunzira za mavutowo?

(1) ____________

(2) Ife sitiyenera kuchita mantha.

========================================================================

8. Chinthu choyamba chimene timaphunzira ndi chakuti Yesu adzakhala ndi ife. Taphunzira kuti ife sitiyenera kuchita mantha pamene mavuto adza. Yesu anasamalira ophunzira. Iye analetsa mphepo yaikulu. Yesu ali ndi mphamvu pa zinthu zonse. Akuphunzira anali kuchita mantha pamene madzi anali kuloŵa mngalawa.

Mwina ophunzira anali kudabwa kuti vutoli labwera bwanji kwa iwo chifukwa chiyani?

____________

Kodi ophunzira anali kuchita zimene Yesu anaŵauza kuti achite? ____________

Kodi chinaoneka ndi chiyani kwa iwo pamene anamvera Yesu? ____________

____________

========================================================================

9. Akuphunzira anachita zimene Yesu ananena. Koma pamene iwo anali kumvera, vuto lalikulu linafikira iwo. Mwina inu muli kuganiza kuti Yesu sanayenere kuuza akuphunzira kuti atsogole ndi ngalawa. Ngati Yesu anadziŵa zinthu zonse, anadziwa kuti mphepo inali kubwera. Mwina Iye akadayenera kuŵasunga ophunzira kuti asaloŵe m'mavuto. Ine ndikuganiza kuti Yesu analola kuti iwo akumane ndi mavuto kuti akhoze kuona mphamvu zina zodabwitsa.

Kuchokera pa nthaŵi imene Yesu anayenda pamadzi, kodi ife timaphunzira chiyani za mavuto?

(1) ______________________________

(2) ______________________________

==================================================================

10. Poyamba taphunzira kuti Yesu adzakhala nafe. Iye adzabwera kwa ife pa nthaŵi ya mavuto a akulu. Chinthu chachiŵirichi taona kuti ife sitiyenera kuchita mantha. Taona kuti Yesu anaonetsa mphamvu yake yaikulu pochulukitsa chakudya chochepa cha mnyamata. Mphunziro lalero Yesu ali kuonetsa mphamvu yake yaikulu. Iye anaonetsa ophunzira ake poyenda pamwamba pamadzi. Iye anaonetsa poletsa mphepo.

Kodi ophunzira anali otani pamene anali ndi mavuto a akulu?

______________________________

==================================================================

11. Iwo anali kuchita mantha. Mavuto amabweretsa madandaulo ndi mantha Mwina inu munali ndi mavuto a akulu. Mwina linali monga mphepo yaikulu imene akuphunzira anali nalo. Kodi inu munali kuchita mantha kapena kudandaula? Kodi mukukumbukira kuti Yesu ali ndi mphamvu yaikulu?
Kapena tsopano muli ndi mavuto a akulu. Mawu a Yesu ndi a inunso. Yesu ali kunenanso kwa inu monga momwe anauzira ophunzira.

Marko 6:50:

> Koma pomwepo anaŵalankhula nanena nawo, "Limbani mtima ndinetu, musaope."

Kodi Yesu amanena chiyani kwa ife pamene tiri m'mavuto?

______________________________

12. Iye anati, Limbani mtima. Ndine. Musaope. Ine ndiri ndi bwenzi amene anali ndi mavuto a akulu. Iye ndi wophunzira Buku Lopatulika ku Seminare ya ku Nigeria. Mkazi wake anali wodwala kwambiri pamene anabereka mwana wawo woyamba.

Mwana anali bwino. Koma mayiyo sanali kutha kudya kapena kulankhula. Iye sakanakhoza kusamalira mwanayo. Iye anangokhala m'chipatala kwa miyezi isanu ndi iŵiri. Potsiriza anamwalira. Ine nditsimikiza kuti bwenzi langa nthaŵi zina anali kuchita mantha. Iye sanadziŵe chifukwa chimene vutoli linadza kwa iye. Koma iye sanadandaule. Bwenzi langa anadziŵa kuti Yesu anali naye m'mavuto ake onse. Iye anadziŵa kuti Yesu ananena kuti, "Usaope." Bwenzi langa anakonda Yesu kwambiri kuposa pa nthaŵi imene mavutoŵa asanabwere.

Pamene ife tiri m'mavuto, kodi ife tiyenera kuchita mantha kapena kusachita mantha?

________________________________________

________________________________________

==========================================================================

13. Ife sitiyenera kuchita mantha. Yesu anafuna kuti ife tizikhala olimba mtima pamene mavuto adza kwa ife. Yesu anauza ophunzira ake kuti apite tsidya lina la nyanja. Iwo anachita monga zomwe Yesu anawauzira. Mphepo inabwera pamene iwo anali kumvera Yesu. Bwenzi langa anachitanso zimene Yesu anamuuza kuti achite. Iye anapita ku sukulu ya Seminare ya Buku Lopatulika. Iye anali kukonzekera kuti akhale mbusa pamene mkazi wake anafa. Iye anamvera Mulungu, koma iye anali ndi mavuto. Yesu anafuna kuti atiphunzitse ife.

Kuchokera pa nthaŵi imene Yesu anayenda pamadzi ndi kutontholetsa mphepo kodi timaphunzira chiyani za mavuto.

(1) Yesu adzakhala nafe.

(2) ________________________________________

==========================================================================

14. Ife sitiyenera kukhala ndi mantha. Pamene zinthu zovuta zabwera, anthu ena amadana ndi Mulungu. Ena amasiya kupita ku tchalitchi. Pamene mavuto abwera, iwo samamvera Yesu. Iwo samamvera Iye ali kunena kuti, "Ndine, musaope." Yesu ndi wokonzekera kunena mawu ameneŵa kwa amene ali m'mavuto.

15. Iye amanena zimenezi kwa ife. Iye ali kunena zimenezi kwa inu. Iye ali kunena zimenezi kwa Akhristu amene ali m'mavuto. ɔ.

Kodi ndi chinthu choyamba chotani chimene timaphunzira kuchokera ku chozizwitsa pamene Yesu anayenda pamadzi ndi kuletsa mphepo?

___

===

16. Timaphunzira kuti Yesu adzakhala ndi ife. Lero tikuphunzira zozizwitsa ziŵiri. Yesu anayenda pamadzi ndipo anatontholetsa mphepo. Zozizwitsa zimenezi zimatithandiza ife kudziŵa kuti Yesu amakonda anthu ndi kuti ali ndi mphamvu yaikulu.

Kuchokera pa zozizwitsa za kuti Yesu anayenda pamadzi ndi kuti anatontholetsa mphepo, kodi timaphunzira chiyani za mavuto?

(1) Yesu adzakhala nafe

(2) ___

===

17. Timaphunzira kuti tisamachite mantha. Chimenechi chimatikumbutsa za mawu a Davide.

Masalmo 23:4:

> Inde, ndingakhale ndiyenda m'chigwa cha mthunzi wa imfa,
> sindidzaopa choipa; pakuti inu muli ndi ine.

Ganizirani za chinthu chimodzi chovuta chimene chinakuonekerani, kodi Yesu amabwera pafupi nanu?

___

Lembani mmene Yesu anakuthandizirani ndi zimene anakuphunzitsani?

___

===

18. Mwina mukhoza kugawirana zimenezi wina ndi mnzake mkalasi.

Kuchokera pa zozizwitsa zimene Yesu anayenda pamadzi ndi kutontholetsa mphepo, kodi ife timaphunzira chiyani za mavuto?

(1) ______________________________________________

(2) ______________________________________________

SABATA LA KHUMI: KHRISTU, MKATE WA MOYO
TSIKU LACHITATU: "IDYANI THUPI LANGA NDIPO IMWANI MWAZI WANGA."

1. Lero tikuphunzira mawu ofunika kwambiri a Yesu. Poyamba tiyeni tikumbukire zomwe tinaphunzira dzulo.

Kuchokera pa zozizwitsa zomwe Yesu anayenda pamadzi ndi kuletsa mphepo, kodi ife timaphunzira chiyani za mavuto?

(1) ______________________________

(2) ______________________________

==========================================================

2. Taphunzira kuti Yesu adzakhala ndi ife. Taphunzira kuti sitiyenera kuchita mantha. Yesu amasamala pa zosoŵa za anthu. Iye anathandiza ophunzira m'mavuto awo. Iye anadyetsa unyinji wa anthu okwanira zikwi zisanu pamene iwo anali ndi njala.

Ambiri mwa anthu amene anadyetsedwa anabwera kudzamva mawu a Yesu. Iwo anafuna chakudya china chambiri. Yesu anaŵaphunzitsa phunziro la mkate. Iye anawaphunzitsa iwo za mkate woona wochokera kumwamba. Iye anati ayenera kudya thupi lake ndi kumwa mwazi wake. M'mawu ameneŵa Yesu anatanthauza kuti:

(1) Ife tiyenera kulandira Yesu m'miyoyo yathu.

(2) Tiyenera kutenga mphamvu kuchokera kwa iye tsiku ndi tsiku.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Yohane 6:17 mpaka 57. Ŵerenganinso ndime 48. Kodi Yesu anadzitcha chiyani m'ndime imeneyi?

______________________________

==========================================================

3. Yesu anadzitcha yekha mkate wamoyo. Ife timadya mkate kapena chakudya tsiku ndi tsiku. Ngati titapanda kudya, timamva njala kwambiri, ndipo pasanapite nthaŵi tikhoza kufa. Yesu anati, ife tilandire Yesu kuti tiyambe moyo wathu wa Uzimu.

Yohane 6:26-27:

Yesu anayankha iwo nati, "Indetu, indetu, ndinena ndi inu, mundifuna Ine sichifukwa munaona zizindikiro koma chifukwa munadya mkate nimukhuta. Gwirani ntchito si chifukwa cha chakudya chimene chitsalira ku moyo wosatha chimene mwana wa munthu adzakupatsani inu.

Kodi anthu anapeza chiyani kuchokera kwa Yesu pamene Iye anadyetsa anthu zikwi zisanu?

_______________________________________________

_______________________________________________

==========================================================

4. Iwo anapeza chakudya kuchokera kwa Yesu. Iwo anapeza mkate ndi msomba. Iwo anadya zambiri pa tsiku limenelo. Anabweranso kudzafuna zina zakudya. Koma Yesu anati anthu sayenera kugwira ntchito chifukwa cha chakudya chimene chimaononongeka. Iwo anayenera kugwira ntchito chifukwa cha chakudya chimene chimapatsa moyo wosatha.

Yohane 6:53:

Yesu anati kwa iwo, Indetu, indetu, ndinena ndi inu ngati simukudya thupi la mwana wa munthu ndi kumwa mwazi wake, mulibe moyo mwa inu nokha.

Kodi ife tingaletse bwanji njala imene timamva m'matupi athu?

_______________________________________________

==========================================================

5. M'malo mofuna kuletsa njala yathu, tiyenera kudya chakudya. Pamene munthu ali ndi njala kwambiri, iye akhoza kupita nakaonera wina ali kuphika chakudya. Koma iye adzakhalabe ndi njala. Iye akhoza kupita ku sitolo ndi kukayang'anira pa mkate umene uli kugulitsidwa. Koma iye adzakhalabe ndi njala. Munthu ayenera kupeza chakudya. Iye ayenera kudya chakudyacho ndi kumeza.

Pamene Yesu akuti ife tiyenera kumudya Iye, kodi tiyenera kumulandira Iye m'chiyani?

_______________________________________________

_______________________________________________

6. Tiyenera kumulandira Iye m'miycyo yathu. Kungodziŵa za Yesu kokha sikukwanira. Kuganizira za Yesu sikukwanira. Kukhulupirira kupyolera m'kanthu kena za Yesu sikukwanira. Iye amafuna kudza m'ziwalo zonse za thupi ndi m'maganizo anu.

Kodi timati tikuchita chiyani ndi thupi la Yesu ndi mwazi wake pamene timulandira Iye m'miyoyo yathu?

---

7. Ife timati "tikudya thupi ndi kumwera mwazi wake." Ngati ife sitichita zimenezi tilibe moyo wa Uzimu.

Yohane 6:50-51:

> Mkate wotsika kumwamba ndi uwu, kuti munthu akadyeko ndi kusamalira. Mkate wamoyo wotsika kumwamba ndine amene. Ngati munthu wina akadyako mkate umene, adzakhala ndi moyo wosatha.

Pamene tidya thupi lake ndi kumwera mwazi wake, kodi timalandira ndani m'miyoyo yathu?

---

8. Ife timalandira Khristu. Pamene tichita zimenezi tidziŵa kuti sitidzafa.

Yohane 6:53-54:

> Indetu, indetu, ndinena ndi inu, ngati simukudya thupi la mwana wa munthu ndi kumwa mwazi wake, mulibe moyo mwa inu nokha. Iye wakudya thupi langa ndi kumwa mwazi wanga ali nawo moyo wosatha; ndipo Ine ndidzamuukitsa iye tsiku lomaliza.

Kodi chinthu choyamba chimene Yesu anatanthauza chinali chiyani pamene ananena kuti, "Idyani thupi langa ndipo mwerani mwazi wanga?"

(1) ______________________________

(2) Ife tiyenera kukhala ndi mphamvu ya uzimu kuchokera kwa Iye tsiku ndi tsiku.

---

9. Iye anatanthauza kuti tiyenera kumulandira m'miyoyo yathu. Munthu aliyense m'dziko lapansi ayenera kuchita chimenechi. Mwina inu simunalandire Yesu m'moyo mwanu. Ngati izi ziri zoona tsopano mukhoza kuweramitsa mutu wanu. Mukhoza kumulandira Iye tsopano m'moyo wanu.

Ngati munalandira kale Yesu, uzani bwenzi lanu phunziroli. Ganizirani za munthu wina amene sanalandire Yesu m'moyo mwake. Pitani mukamuuze zimene mwaphunzira mphunziro limeneli. Lembani dzina la bwenzi amene inu mwakonzekera kukamuuza za Yesu.

____________________________________

===========================================================================

10. Pa nthaŵi ya kalasi yanu ina tidzalankhulana za chimenechi. Inu mukhoza kudzanena za mmene inu munamuuzira za phunziro ndi wina wake.
Koma mawu akuti "Idyani thupi langa ndi kumwa mwazi wanga" ali ndi chifukwa chinanso. Iwo amatanthauza kuti tizitenga mphamvu kuchokera kwa Yesu tsiku ndi tsiku.

Yohane 6:55-56:

> Pakuti thupi langa ndi chakudya ndithu ndi mwazi wanga ndi chakumwa ndithu. Iye wakudya thupi langa ndi kumwa mwazi wanga akhala mwa Ine ndi Ine mwa iye.

Kodi ndi ndani amakhala mwa ife ngati titadya thupi lake ndi mwazi wake?

________________________________________

===========================================================================

11. Yesu amakhala mwa ife. Kukhala kumatanthauza kuti Iye ali mkati mwathu. Yesu analankhula za zimenezi pa Yohane 15. Iye anafuna kuti ife timvetsetse.

Yohane 15:4-5:

> Khalani mwa Ine ndi Ine mwa inu. Monga nthambi siingathe kubala chipatso payokha, ngati siikhala mwa mpesa; motero mulibe inunso ngati simukhala mwa Ine. Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zake; wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala chipatso chambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kuchita kanthu.

Kodi nthambi ikhoza kupeza mphamvu yogwirira ntchito yake motani?

______________________________________________________________________